Adamu?
-Mkazi woyamba, Hava.

59. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulenga Hava?
-Chifukwa chakuti Mulungu anamukonda Adamu.
-Chifukwa chakuti Mulungu samkafuna kuti Adamu adzikhala yekha.
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kuti Adamu ndi Hava abereke ana.

60. Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkayenda ndi Mulungu, kodi amkakhala bwanji?
-Pachiyambi, Adamu ndi Hava amkayenda ndi Mulungu, ndipo anali osangalala kwambiri.



PHUNZIRO LA 10

1. Kodi ndi mawu a ndani amene ali ofunika kwambiri kuposa mawu ena aliwonse pa dziko la pasi?
-Mawu a Mulungu.

2. Kodi chifukwa chiyani mawu a Mulungu ndi ofunika kwambiri kuposa mawu ene aliwonse pa dziko la pasi pano?
-Chifukwa chakuti anthu onse ananamako.
-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene sananameko.
-Chifukwa chakuti ndi Mulungu yekha amene amanena zowona zenizeni.

3. Kodi ndi ndani amene analipo, dzikoli lisanapangidwe?
-Mulungu.

4. Kodi chiyambi cha Mulungu chinali liti?
-Mulungu alibe chiyambi.

5. Kodi pali munthu amene anamulenga Mulungu?
-Palibe.
-Mulungu ndi wachikhalile mpaka kalekale.

6. Kodi Mulungu anamulenga Mulungu?
-Iyayi.
-Mulungu ndi wachikhalile mpaka kalekale.

7. Kodi pali munthu amene anamubereka Mulungu?
-Palibe.
-Mulungu ndi wachikhalire mpaka kalekale.

8. Kodi Mulungu anamulenga Mulungu?
-Iyayi.
-Mulungu ndi wachikhalire mpaka kalekale.

9. Kodi pali nthaŵ i imene Mulungu kunalibe?
-Palibe.
-Mulungu ndi wachikhalire mpaka kalekale.

10. Kodi Mulungu amasintha?
-Iyayi.
-Mulungu sasintha.

11. Kodi Mulungu angafe?
-Iyayi.
-Mulungu sangafe.

12. Kodi Mulungu ali ndi mnofu ndi mafupa ngati anthu?
-Iyayi.
-Mulungu ndi Mzimu.

13. Anthu amafuna chakudya ndi madzi kuti akhale ndi moyo, kodi nanga Mulungu amafuna chiyani?
-Mulungu safuna china chilichose kuti akhale ndi moyo.

14. Kodi nanga Mulungu amakhala bwanji ndi moyo?
-Mulungu amakhala ndi mphamvu Yake.

15. Kodi Mulungu ali kuti?
-Mulungu ali palipose nthaŵ i zonse.

16. Kodi pali Milungu yingati?
-Pali Mulungu m'modzi yekha.

17. Kodi atatu amene ali Mulungu m'modzi ndi ndani?
-Mulungu Atate, Mulungu Mwana (Mpulumutsi) ndi Mulungu Mzimu Woyera.

18. Kodi ndi ndani amene analenga dziko la pasi ndi kum-



-Mulungu anaŵalenga anthu onse abwino.

51. Mulungu anamulenga Adamu, kodi Iye anamuwuza Adamuyo kuti adziyang'anira chiyani?
-Mulungu anamupatsa Adamu udindo oyang'anira dziko lonse la pasi ndi zinthu zonse zopezeka m'menemo.

52. Kodi Mulungu atatha kumulenga Adamu, anamuyika kuti?
-M'munda mwa Edeni.

53. Kodi dzina la mtengo woyamba umene Mulungu anawudzala pakati pa munda wa Edeni linali chiyani?
-Mtengo Wopereka Moyo.

54. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anadzala Mtengo Wopereka Moyo pakati pa munda wa Edeni?
-Mulungu amkafuna kuti Adamu adzidya zipatso za mu mtengowo kuti akhale moyo mpaka kalekale.

55. Kodi dzina la mtengo, chipatso chimene Mulungu anamulamula Adamu kuti asadye linali chiyani?
-Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa.

56. Kodi Adamu anakadya kuchokera mu Mtengo Wodziwitsa Zabwino ndi Zoyipa, chinakamuchitikira ndi chiyani?
-Adamu anakafa.

57. Kodi imfa ndi chiyani?
-Imfa ndi kusiyana ndi Mulungu, wopereka moyo.
-Imfa ndi kusiyana kwa thupi ndi moyo.
-Imfa ndi kusiyana kopita ku Nyanja ya Moto wosatha.

58. Kodi Mulungu anamulenga ndani kuti adzimuthandiza

-Satana.

43. Kodi dzina lakuti “Satana” limatanthawuza chiyani?
-Limatanthawuza kuti “mdani.”

44. Kodi dzina latsopano la angelo amene anamutsatila Lusifala ndi ndani?
-Ziwanda.

45. Kodi Mulungu anakhonza malo anji a chilango kwa satana ndi ziwanda zake?
-Nyanja ya Moto Wosatha.

46. Kodi Satana ndi ziwanda zake zimalimbana ndi ndani?
-Satana ndi Ziwanda zake zimalimbana ndi Mulungu ndi ntchito Yake yonse.

47. Kodi Mulungu atatha kukomza dziko la pasi, analenga ndani?
-Adamu, mamuna woyamba.

48. Kodi Mulungu anaŵalenga bwanji anthu mosiyana ndi nyama?
-Mulungu anaŵalenga anthu mu chifaniziro Chake.

49. Kodi zikutanthawuza chiyani kuti Mulungu analenga munthu mu chifaniziro Chake.
-Mulungu anaŵapatsa anthu mzeru kuti adzimudziwa Iye.
-Mulungu anaŵapatsa anthu maganizo a mphamvu kwambiri kuti adzimukonda Iye.
-Mulungu anaŵapatsa anthu chifuniro kuti adzisankha kumumvera Iye.

50. Kodi Mulungu anaŵalenga anthu abwino kapena oyipa?



wamba?
-Mulungu.

19. Kodi Mulungu anagwiritsa ntchito chiyani polenga dziko la pasi?
-Mulungu sanagwiritse ntchito china chilichose.
-Mulungu analenga dziko la pasi ndi kumwamba posagwiritsa ntchito china chilichonse.

20. Kodi Mulungu anazilenga bwanji zinthu zonse?
-Pongolankhula.

21. Kodi Mulungu anatha bwanji kulenga kumwamba ndi dziko la pasi?
-Mulungu ndi wa mphamvu zonse.
-Mphamvu za Mulungu sizitha.
-Palibe china chilichonse chimene Mulungu angalephere kuchichita.

22. Kodi Mulungu anadziŵ a bwanji malengedwe a dziko la pasi ndi kumwamba?
-Mulungu amadziwa zinthu zonse.
-Mzeru za Mulungu zilibe malire.
-Palibe chimene Mulungu sachidziŵ a.

23. Kodi Mulungu anati chiyani pa zinthu zonse zimene Iye anazilenga?
-Mulungu anati kuti zinthu zonse zinali zabwino.

24. Kodi Mulungu anatha bwanji kulenga zinthu zonse zabwino zokhazokha?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi wabwino kwambiri.

25. Kodi Mulungu anamulengera ndani zinthu zonse?
-Anaŵalengera anthu.

26. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anaŵalengera anthu zinthu zonsezi?
-Chifukwa chakuti Iye amatikonda ife kwambiri.

27. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi amene ali oyenera kukhala mwini wa zinthu zonse?
-Chifukwa chakuti Iye ndi amene analenga zinthu zonse.

28. Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi amene ali ndi udindo wakutilamula ife tonse kuti tidzimumvera?
-Chifukwa chakuti Iye ndi amene anatilenga ife tonse ndi kutipatsa moyo.

29. Kodi angelo onse anachokera kuti?
-Analengedwa ndi Mulungu.

30. Kodi Mulungu anaŵalenga angelo ndi kuŵ apatsa minofu ndi mafupa?
-Iyayi.
-Mulungu anaŵalenga angelo ngati mizimu.

31. Kodi Mulungu anaŵalenga angelo ena oyipa ena abwino?
-Iyayi.
-Mulungu anaŵalenga angelo onse abwino.

32. Kodi Mulungu anaŵalenga angelo chifukwa chakuti amkafuna chithandizo?
-Iyayi.
-Mulungu samafuna chithandizo.

33. Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu analenga angelo?
-Chifukwa chakuti anaŵakonda angelowo.



34. Pachiyambi, kodi angelo amkakhala kuti?
-Amkakhala kumwamba ndi Mulungu.

35. Kodi angelo akhoza kupezeka pena palipose pa nthaŵ i imodzi?
-Iyayi.
-Mulungu yekha ndi amene amatha kukhala pena palipose pa nthaŵ i imodzi.

36. Kodi ndi ndani amene Mulungu anamulenga kuti akhale wamkulu wa angelo onse?
-Lusifala.

37. Pachiyambi, tsiku lina kodi Lusifala anachita chiyani?
-Lusifala anaziwona mzeru ndi mphamvu zimene anali nazo ndipo anayamba kudzikweza.

38. Kodi Lusifala anaganiza zochita chiyani?
-Lusifala anaganiza zomuchotsa Mulungu pa udindo Wake.

39. Kodi Mulungu anamulola Lusifala kuti amuchotse Iye pa udindo Wake?
-Iyayi.

40. Kodi Mulungu anachita chiyani atakwiya ndi Lusifala?
-Mulungu anamuchotsa Lusifala kuchokera kumwamba.

41. Kodi Mulungu anachita chiyani atakwiya ndi angelo amene anamutsatira Lusifala?
-Mulungu anaŵachotsanso angelowo kuchokera kumwamba.

42. Kodi dzina latsopano la Lusifala ndi ndani?